

Kukwatitsa ndi Kuphukitsa Zomela

Ndondomeko ya malangizo a alimi ang'no-ang'ono

Kodi kukwatitsa zomela n'kutani?

Kukwatitsa comela ndi njila zosiyana-siyana zimene amadula mbali ya nthambi ili ndi mphukila n'kuiphatikiza kapena kulumikiza panthambi ina (thunthu) ya mtundu wa mtengo wina. Conde dziwani kuti kukwatitsa comela kungaphatikizeponso kulumikiza nthambi zambili ku thunthu imodzi.

Kodi kuphukitsa zomela n'kutani?


Kuphukitsa comela kumatanthauza njila zambili zimene mphukila imodzi kapena zambili kucokela kumtengo umene mufuna n'kuphatikiza/kulowetsa panthambi mwang'amba kapena kulumikiza ku thunthu yamtengo wa mtundu wofanana...

Mapindu a kukwatitsa ndi kuphukitsa zomela?

- ▶ Mitengo yokwatitsa kapena kuphukitsa imabala zipatso mwamsanga. Mtengo womela kucokela ku njele ungatege zaka 8 mpaka 10 kuti ubale, koma wokwatitsa umatenga zaka cabe 2 mpaka 4.
- ▶ Mtengo wobzalidwa kucokela ku njele sumabeleka zipatso monga mmene mtengo munatengako njele(cimake ca mtengo). Koma mtengo wokwatitsa kapena wophukitsa udzakhala n'zipatso zabwino cimodzimidzi monga mtengo munadulako mbewu (mphukila).
- ▶ Kukwatitsa ndi kuphukitsa zomela kumathandiza kulimbisa mitengo ku tulombo ndi matenda.
- ▶ Mbewu yokwatitsa imakula msanga poyelekeza ndi ija yophukitsa, koma yophukitsa ili ndi ubwino kuposa yokwatitsa ngati palibe mphukila zokwanila mwacitsanzo mphukila ya 25cm ingamele nkomo 8 mpaka 10.

Zitsulo zofunikila pokwatitsa ndi kuphukitsa zomela

Zotsatila n'zitsulo zofunikila pokwatitsa kapena kuphukitsa mbewu:



(a) Pulasitiki yongwelewelela yaulimbo mbali imodzi; (b) citsulo ca mpeni/kalumo; (c) citsulo cothenela maluwa; (d) cida codulila pokwatitsa (e) sipiriti/kacasu ndi thonje; (f) cipula/mpeni cong'ambila pokwatitsa

Promotion of agroforestry supported by:

With support from
Federal Ministry of Food and Agriculture

Prepared by: Daniel M. Kalala

by decision of the German Bundestag

Ndondomeko yotsatila pokwatitsa zomela



1 Kukonzekelelsa mphukila: Gwilitsilani nchito cida cothenela maluwa caukhondo kapena mpeni, dulani mphukila zilibe matenda ndi tulombo. Mphukila zikhale utali wa 10 mpaka 15cm kapena utali wa zanja lanu. Cotsani mayani onse, muonetsetse kuti nsonga yophukila (nkomo) sinavulazidwe.



2 Kulumikiza mphukila pa(ndi) tsinde: Mphukila ndi tsinde zikhale zolinga myezo/ukulu wake. Gombani pakati pa tsinde kupita pansi kugwilitsilani nchito mpeni kapena pangani phanda patsinde(Vshape) kusewenzetsa citsulo cothenela maluwa. Songolani kungsi kwa mphukila. Lowetsani mphukila ija patsinde kuonetsetsa kuti zalumikizana bwino-bwino.



3 Kuteteza ndi kucinjiliza mphukila: Tetezani mphukila mwa kumangilila ndi pulasitiki yongwelewelela yaulimbo mbali imodzi pamfundo mwalumikiza. Phimbani mbande/mbewu yanu ndi pulasitiki kuyambila pamwamba mpaka kupitililako pamfundo pomanga. Pulasitiki imathandiza kusunga mnyonho ndi kutentha kwabwino.

Ndondomeko yotsatila pokhukitsa mbewu



4 Kusunghanitsa mphukila ndi tsinde: Tengani mphukila kucokela pakati pa zitsamba. Mphukila zipezeka kungsi kwa mtengo zimakhala zokalamba ndipo zakunsonga zimakhala zosakhwima/zofewa. Tsinde yophukitsilapo ikhale monga myezo wake. Cotsani mayani onse ali pansi pamfundo mwalumikizila.



5 Kulumikiza mphukila pa(ndi) tsinde: Gwilitsilani nchito mpeni/kapula wong'ambila pokwatitsa kapena kalumo, ng'ambani T patsinde. Lowetsani mphukila poikankhila pansi kupita pamwamba kuonetsetsa kuti pali kulumikizana winobwino pakati pa minyewa/mnofu.



6 Kuteteza mphukila/nkomo: Sewenzetsani pulasitiki kumanga pamwamba ndi pansu pa mphukila kuonetsetsa kuti mphukila yagwila bwino pamalo pake kuti isaume.

Zinthu zoyenela kuganizila pokwatitsa ndi kuphukitsa bwino

Nthawi yokwati

- ▶ Mitengo yazipatso ingakwatitsidwe nthawi zosiyana pacaka malinga ndi njila mudzagwilitsilani nchito.
- ▶ Kukazizila, kuti mbewu zipange bwino konzani malo mofesela mbewu mmene kutentha ndi kuzizila komanso mnyonho zimayanganiidwa.
- ▶ Zotsatila zabwino zimapezeka mnyengo yofunda, yamnyonho.

Nthawi yophukitsa

N'zotheka kuphukitsa zomela caka conse. Komabe, zipatso monga malalanje, mandimu, manyumwa (citrus) nthawi yabwino yophukitsa mu Zambia ndi kuyambila mwezi wa August mpaka November ndi March mpaka April. Sitikulimbikitsa kuphukitsa mbewu munyengo yozizila(June mpaka July).

Ukhondo pokwatitsa ndi kuphukitsa zomela

Kuti mupewe kuipitsa pokwatitsa ndi kuphukitsa, onetsetsani kutimwasamba kumanja ndi sopo komanso sewenzetsani mankhwala ophela tulombo. Zida zonse mudzagwilitsilani nchito zisukidwe ndi mankhwala ophela tulombo/kacasu (methylated spirit).



7 Kasamalilidwe ka kutentha ndi kuthilila mukakwatitsa ndi kuphukitsa: Mukangolumikiza kapena kuphukitsa mbewu, ikani mbande pansu pa mthunzi. Thililani pamlingo wabwino. Musanayambe kubzala mbewu munafesa, yambani kuchepetsa kuthilila n'kuika zomela/mbande padzuwa kwa milungu 6 mpaka 8 kuti zilimbe.



8 Kusamalila pambuyo pokwatitsa ndi kuphukitsa: Pambuyo pa milungu iwili mukakwatitsa, cotsani pulasitiki ngati mphukila zatsopano zaonekela. Ngati siconco, ndipo kamtengo/mpukhila kakali kobiliwila, cotsani pulasitiki pamene mphukila zipanga. Nthawi zambili, pulasitiki yongwelewelela yaulimbo mbali imodzi ikagwilitsidwa nchito kumangila mfundo kapena mphukila imacoka yokha, koma ngati n'pulasitiki wamba/ina-iliyonse, conde cotsani pambuyo pa miyezi 3. Ngati papita milungu iwili mphukila silinso yobiliwila(kuyamba kuoneka bulauni), zitanthauza kuti kukwatitsa sikunali/sikuyende bwino.